

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

PAMENE UCHIMO UNACHULUKA

Dziko lili mundima ndipo uchimo ukuchuluka. Malingaliro ndi mitima ikuchititsidwa khungu ndi zikhumbitso ndi zilakolako zathupi. Dzikoli likunka lisendera kutali ndi chiyero cha Mau a Mulungu. Iwo amene amadzitcha Akhristu akuvomereza kaganizidwe kachilendo ka dzikoli. Ukwati sukulemekezedwanso monga kudzipereka kwa moyo wako wonse, ndipo sukuonedwanso ngati ubale wamuyaya pakati pa mwamuna ndi mkazi. Kodi pali chiyembekezo chotani mu mbadwo uno wosaopa Mulungu?

Zaka zapitazo, mbusa wina analowa m'chipinda chogona odwala cha chipatala china mmene munali mnyamata wina wochita za zogonana amuna okhaokha (zamathanyula) amene anali kumwalira ndi matenda a EDZI. Mnyamatayo, yemwe anali m'masiku otsiriza a moyo wake, anagona pabedi lachipatala atavala chovala cha pinki. Mbusayo anampempha kuti acheze naye.

Mnyamatayo anayankha kuti “Sindikufuna kulankhula nanu, mukufuna kungondiuzi kuti ndikafa ndidzapita ku gehena.”

Mbusayo anayankha kuti, “Ai, ndikufuna kukuuza za chikondi cha Mulungu pa iwe.”

Mbusayo atayamba kucheza ndi mnyamata wochita za mathanyulayu, anamuuzza zachikondi chodabwitsa cha Mulungu popeza iye amakhala m'moyo wochimwa kwambiri. Anamuuzza za choonadi chokoma chopezeka pa Yohane 3:16-17. “Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. Pakuti Mulungu sanatume Mwana wake kudziko lapansi, kuti akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi likapulumsidwe ndi Iye.”

Pamene mbusayo amakamba za chikondi cha Yesu ndi mmene Iye anadzera

kudzatipulumutsa ku machimo athu, misozi inatsika m'maso mwa munthu wotsala pang'ono kufayo. Anapemphera kwa Yehova ndi kupempha Mulungu kuti amukhululukire machimo ake onse. Pa nthawiyo, mnyamatayo anakhala wolengedwa watsopano mwa Yesu Khristu. Zakale zonse zinapita ndipo zonse zinakhala zatsopano (2 Akorinto 5:17). Nkutheka kuti anakanidwa ndi a m'banja lake, anavutitsa kwambiri anthu amene ankakhala naye pafupi, mwina ankakhala moyo wauchimo kwambiri komanso wakhalidwe lotayirira, koma Mulungu ankamukonda ndipo anamulandira. Iye anasambitsidwa ndi mwazi wa Yesu Khristu ndi kuyeretsewda.

Nthawi yomweyo mnyamatayo anaitana namwino nkumupempha kuti amupatse chovala cha odwala a m'chipatalamo. Ichi chinali chizindikiro chochepe chabe choonetsera kulapa kwenikweni kwa munthuyu pamaso pa Mulungu. Adamupempha mbusayo kuti adzalalikire pamaliro ake ndipo anati, “Pamaliro anga padzakhala anzanga ambiri ochita zogonana amuna kapena akazi okhaokha. Ndikufuna mudzawauze zimene mwandiuzazi. Mudzawauze kuti Mulungu amawakonda!”

Ha! Aleluya, alemekezeke Mulungu! Monga momwe Davide ananenera, “Koma kwa Inu kuli chikhululukiro” (Salmo 130:4). Chikondi ndi chikhululukiro cha Yesu zimaperekedwa kwa aliyense mpaka lero, mosawerengera kanthu kuti uchimowo ndi waukulu motani kapena munthu wadwala motani. “Yesu anadza kudziko lapansi kupulumutsa ochimwa” (1 Timoteo 1:15).

Panali mzimai amene atsogoleri achipembedzo anabwera naye kwa Yesu. Iye anagwidwa akuchita chigololo ndipo amayenera kuti aweruzidwe ndi kupatsidwa chilango chakuti

(Yapitirira pa tsamba 2)



“Chikondi ndi chikhululukiro cha Yesu zimaperekedwa kwa aliyense mpaka lero, mosawerengera kanthu kuti uchimowo ndi waukulu motani kapena munthu wadwala motani.”

Mau a Mkonzi

3

Kalozera pophuzira Baibulo

4

Kugonana kwa Amuna Kapena Akazi Okhaokha ndi Kupatuka

5-6

Funso Yanko

7

Kodi Mukudziwa?

Mau a Nyengo Yake

8

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

aphedwe. Komabe Yesu anamuza kuti, “Inenso sindikutsutsa iwe; pita; kuyambira tsopano usachimwenso” (Yohane 8:11). Pakati pa ziweruzo za anthu ena, iye adapeza kulandirika mwa Yesu. Iye anamupatsa chiyembekezo ndipo sanamusiye mu uchimo wakewo. Pamene dziko likunena kuti chikondi cha Yesu chimafungatira uchimo, chikondi chenicheni ndi mphamvu za Yesu zidzawachotsa iwo kuchoka ku uchimo kuti anthu apite ndipo asakachimwenso.

Panalinsu mzimai wina amene Khristu anakumana naye pachitsime. Iye anati alibe mwamuna. Yesu anamuza iye kuti ananena molondola, “pakuti wakhala nao amuna asanu; ndipo iye amene ukhala naye tsopano sali mwamuna wako” (Yohane 4:18). Yesu anamuza za madzi amoyo amene akhoza kuthetsa ludzu la moyo. Anthu ambiri ali ngati

“Anthu akufunafuna
zosangalatsa ndi zilakolako
zathupi pofuna kuti apeze
cholinga m’moyo, adziwike
ndipo akhutitsidwe.”

mzimai ameneyu. Kusintha zibwenzi komanso ocheza nao sikunakhutitse chikhumbo chake. Anthu akufunafuna zosangalatsa ndi zilakolako zathupi pofuna kuti apeze cholinga m’moyo, adziwike ndipo akhutitsidwe. Chifukwa chakuti zinthu zimenezo

sizikhutitsa, anthu amazamirizamira mu uchimo, kufunafuna mtendere weniweni koma osaupeza. Yesu anabwera kudzatumikira ku chosowa cha moyo. Pamene anthu adzipereka kwa Yesu Khristu, nasiya machimo ao, adzapeza mtendere weniweni ndi kulandiridwa.

Mtumwi Paulo analankhula kwa Akhristu a ku Korinto za iwo amene sadzalowa Ufumu wa Mulungu: adama, achigololo, ogonana amuna kapena akazi okhaokha, oledzera, ndi ena otero. Iye anati, “Ndipo ena a inu munali otere; koma munasambitsidwa, koma munayeretsedwa” (1 Akorinto 6:11). Awa ndi mau okoma kwambiri kuwamva mu nyengo ino yoipa. “Ndipo ena a inu munali otere; koma...” Ziliba kanthu kuti munthu wakhala akuchimwa motani kapena akuyenda m’moyo wotani, chipulumutso chilipo kwa cha onse.

“Pamene uchimo unachulukuka, pomwepo chisomo chinachulukuka koposa” (Aroma 5:20). Chisomo cha Mulungu ndi champhamvu kwambiri kuposa zilakolako zonse ndi ukapolo wa thupi. Chifukwa chake, pitani mukawauze. Pitani mukaliuze dziko za chikondi cha Mulungu. Kawauzeni za chipulumutso. Kawauzeni za chiyembekezo ndi mtendere zimene zili mwa Yesu Khristu! ■

“Amuna amatenga mbali ya azimai,
ndipo azimai omwe amatenga mbali ya amuna,
mosiyana ndi chilengedwe.

Amai nthawi yomweyo ali akazi komanso amuna....

Ha chochititsa manyazi kuchiona! Khalidwe loipa! ”

CLEMENT WAKU ALEXANDRIA
(Mkulu mu mpingo woyamba, cha m'ma 195 AD)

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani.

—Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Pakuti idzafika nthawi imene sadzalola chiphunzitso cholamitsa; komatu poyabwa m'khutu adzadziunjikitsa aphunzitsi monga mwa zilakolako za iwo okha: ndipo adzalubza dala pachoonadi, nadzapatukira kutsata nthano zachabe. — 2 Timoteo 4:3-4

Paulo analimbikitsa Timoteo kuti alalikire Mau. Mulungu atithandize tonsefe kuti tikhalebe okhulupirika pa kulalikira, kuphunzitsa, ndi kukhala ndi moyo mwa Mau a Mulungu suipitsidwa. Anthu ambiri masiku ano sakumvera chiphunzitso choona koma amafunafuna atumiki ndi abusa amene angawauze zomwe akufuna m'moyo uno, ngakhale zitakhala kuti zikusemphana ndi choonadi.

Mutu wathu ulendo uno uli pa nkhani yovuta yokhudza kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha (mathanyula). M'mbuyomu, mutu ngati uwu ukanatha kuonedwa ngati wosayenera, koma malingaliro ndi machitidwe a mtunduwu zafala kwambiri padziko pano ndipo iyi ndi nkhani yomwe ana ndi akulu amakumana nayo pafupifupi tsiku lililonse.

Kwa anthu a zaka 11 mpaka 26, pafupifupi 20 mwa anthu 100 aliwonse, kapena kuti mmodzi mwa anthu 5 aliwonse, amadziona kuti amagonana ndi akazi kapena amuna okhaokha, komanso ndi kumagonana ndi wina wosiyana naye chibadwidwe. Ena amakhala ndi chilakolako cha mwamuna kapena mkazi mnzao kuposana ndi wina wosiyana naye, ndipo enanso sakhala ndi chikhumbokhumbo chilichonse cha mkazi kapena mwamuna. Enanso amadzisintha, mwamuna kudziyesa wamkazi ndipo mkazi kudziyesa mwamuna pomwe ena sadziona kuti ali mwamuna kapena mkazi, ndipo ena amadzimva kuli alibe chibadwidwe chilichonse. Iyi ndi nkhani yaikulu mu nthawi yathu ino. Chifukwa cha zinthu zimene zatizungulira zomwe zikutipanikiza kuchokera mu zochitika mdzikoli, achinyamata ambiri adzilimbana ndi mafunso komanso adzikumana ndi mayesero pa nkhani zimenezi.

Pokhala Akhristu, tikambirane nkhaninyi, chifukwa imakambidwanso mu Baibulo. Ngati sitinena za choonadi chimenechi, mau okhawa omwe angamvedwe ndi ochokera ku ziganizo za anthu ochita za mathanyula ndi zikhaliidwe zachilendo zokhudza kugonana komanso chibadwidwe cha munthu. Iwowa akuyesetsa kuti mchitidwe wolakwika wokhudza kugonana udziona kuti ndi mmene zinthu zimayenera kukhalira masiku onse.

Ndinamva chisoni pamene ndinkaphunzira za mutu umenewu pamene ndinawerenga za mmene anthu odzitcha Akhristu akupotozera ndi kusintha tanthauzo la malemba omveka bwino pankhaninyi ndi cholinga chakuti avomereze ndi kumachita nao makhalidwe a uchimowa. Ifeyo tiyenera kutsatira kwathunthu zimene Mau akunena, popeza tidzayenera kuyankhapo pa izi.

Ndikukumbukira zaka zambiri zapitazo ndikuyankhula ndi mkazi wanga monyoza amuna awiri ochita za mathanyula omwe tinakumana nao ndipo ankagula zovala zachikazi. Ambuye adandizazira ndi kundidziwitsa kuti Iye adawafera iwo. Ndikuyamika chifukwa cha kundikumbutsa kumeneku. Yesu amawakonda, ndipo ife tiyenera kukhala atumiki a chikondi chake.

Pamene anthu akunena motsutsana ndi machitidwe a za mathanyula ndi ena achilendo okhudza kugonana, amatchedwa odana ndi anthu ochita za mathanyula. Chifukwa chakuti timalankhula zoonza za uchimo zisatipangitse kukhala odana ndi anthu ochita za mathanyula kapena kusawamvera chifundo. Anthu enieni a Mulungu amakonda ochimwa ONSE ndipo amawalandira kuti abwere ndi kusinthika ndi uthenga wabwino. Iwowa ali anansi athu, anzathu, ndi abale athu. Nkofunika kukumbukira kuti chifukwa chakuti wina akukhala moyo wauchimo sizitanthauza kuti alibe machitachita ena abwino. Ngakhale kuti timadana ndi uchimo ndi kuyankhula motsutsana nao, komabe timawakonda anthuwo.

Dziko lataya umunthu wake, koma Mau a Mulungu komanso mphamvu ya Yesu Khristu zikhoza kubwezeretsanso chiyeero ndi makhalidwe abwino mkati mwa mitima ya anthu. Aliyense kuti akhale tcheru polimbana ndi malingaliro otairira a kulolerana ndi kuvomereza aliyense. Alandireni anthu koma musavomerezane ndi uchimo ndi mayendedwe amene ali wosemphana ndi pulani ya Mulungu.

Ambuye achitire chifundo dziko lathu lapansi ndi kutithandiza ife kukhala nyali za kuwala, chikondi, ndi chiyeembekezo kwa iwo amene ali otaika.

Michael W. Smith

January 2024



Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.



Kalozera pophuzira Baibulo

Mutu: Kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha komanso kupatuka

Kuwerenga Malemba: Kapena simudziwa kuti osalungama sadzalandira ufumu wa Mulungu? Musasocheretsedwe; adama, kapena opembedza mafano, kapena achigololo, kapena olobodoka ndi zoipa, kapena akudziiipsa ndi amuna,...sadalowa Ufumu wa Mulungu. — 1 Akorinto 6:9-10

Mwachidule: Malemba amaphunzitsa kuti kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha ndi tchimo. Kukhala pa chibwenzi kapena kuyanjana ndi munthu yemwe muli ofanana chibadwidwe, kaya ndi mwamuna kapena mkazi, kuli kotsutsana ndi chilengedwe komanso dongosolo la Mulungu la ukwati. Mulungu analenga mwamuna ndi mkazi; ndipo kuyesera kusintha chibadwidwe cha munthu chokhudza kugonana zili zosemphana ndi dongosolo loikidwiratu la Mulungu. Yesu amawakonda ndipo anawafera komanso amafunitsitsa gulu la anthu ochita za mathanyula komanso zikhalidwe zogonana zodabwitsa kuti apulumuke.

I. Muyeso wa choonadi

- A. 2 Timoteo 3:16 Malemba aperekedwa ndi Mulungu.
- B. Yohane 8:32 Choonadi chimabweretsa ufulu.
- C. Yesaya 5:20-21 Tsoka kwa iwo amene atchula choipa kuti chili chabwino.

II. Chipangano Chakale chimadzudzula kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha komanso kugonana ndi nyama

- A. Levitiko 18:22-24 Usamagonana ndi mwamuna monga amagonana ndi akazi.
- B. Levitiko 20:13-16 Kugonana amuna kapena akazi okhaokha kapena kugonana ndi nyama zili zonyansa.

III. Makhalidwe ochita za mathanyula ndi otsutsana ndi chiphunzitsa cha Chipangano Chatsopano

- A. Aroma 1:24-28 Mchitidwe ogonana amuna kapena akazi okhaokha ndi wachiwerewere, wonyansa, komanso wotsutsana ndi chilengedwe.
- B. 1 Akorinto 6:9-11 Odzikongoletsa ndi odzizunza okha ndi anthu.
- C. 1 Timoteo 1:9-10 Kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha ndi kusakhala ndi umulungu.

IV. Chiwerewere chili tchimo

- A. Akolose 3:5-6 Kupha zilakolako zonse zoipa.
- B. Mateyu 15:19-20 Chigololo ndi dama zimaipitsa.
- C. 1 Akorinto 6:18 Ndi kuchimwira thupi.
- D. Agalatiya 5:19-21 Ntchito za thupi.

V. Ukwati uli pakati pa mwamuna ndi mkazi

- A. Genesis 2:18, 22-24 Mulungu analenga mgwirizano wa mwamuna mmodzi ndi mkazi mmodzi.
- B. Mateyu 19:5-6 Mwamuna ndi mkazi ali thupi limodzi.
- C. Aefeso 5:31 Mwamuna ndi mkazi analumikizana.

VI. Kukhala mwamuna kapena mkazi

- A. Genesis 1:27-28 Analengedwa kuti azibala ana.
- B. Mateyu 19:4 Mulungu adalenga mwamuna ndi mkazi.
- C. Duteronomo 22:5 Kuvala zovala zosiyantsa nkonyansa.
- D. 1 Akorinto 6:9 Kukonda zochita zachikazi uli mwamuna—Makhalidwe achilakolako ndi oipa.

VII. Chiweruzo chaumulungu

- A. Genesis 19:1-14 Sodomu ndi Gomora.
- B. Yuda 1:7 Opotokawo adzazunzika ndi moto wosatha.

VIII. Musatsanzire mzimu wa dziko lapansi

- A. Aroma 12:2 Musafanizidwe ndi makhalidwe a pansu pano;
- B. 1 Akorinto 2:12-13 Musalandire mzimu wa dziko lapansi.
- C. 1 Akorinto 3:18-19 Nzeru za dziko lapansi ndi zopusa.
- D. 1 Yohane 2:15-17 Musakonde dziko lapansi.

IX. Mulungu amakonda anthu ochita za mathanyula

- A. Yohane 3:16 Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi.
- B. Aroma 5:8 Pamene tinakali ochimwa, Khristu adatifera ife.

X. Chiyanjanitso ndi chipulumutso cha kwa anthu onse

- A. 1 Yohane 1:9 Mulungu adzatiyeretsa ku chosalungama chilichonse.
- B. 2 Akorinto 5:17-18 Mwa Khristu, zinthu zonse zili zatsopano.
- C. Chivumbulutso 22:17 Aliyense amene afuna.

Kumaliza

Ndipo ena a inu munali otere; koma munasambitsidwa, koma munayeretsedwa, koma munayesedwa olungama, m'dzina la Ambuye Yesu Khristu, ndi mwa Mzimu wa Mulungu wathu. — 1 Akorinto 6:11

KUGONANA KWA AMUNA KAPENA AKAZI OKHAOKHA NDI KUPATUKA

Mulungu waitana anthu ake kuti akhale m'moyo wachiyero, wodzipatula mofanana ndi dongosolo lake la umulungu kwa amuna ndi akazi. Posawerengera zikhalidwe ndi ndale zadziko, zipembedzo zovomereza kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha, Mau a Mulungu amanena kuti zimenezi ndi zikhalidwe zopanda umulungu ndi zochimwa.



Muyezo wa choonadi

Choonadi sichisinthana ngakhale kuti anthu alowerere ndi kutairira. Malingaliro a dziko lapansili amati palibe choonadi chokhazikika koma kuti chikhalidwe chimasinthasinthana. Baibulo ndi Mau ouziridwa a Mulungu (2 Timoteo 3:16) ndipo lili ndi choonadi chokhacho chimene chidzatsogolera anthu pa ulendo wa Kumwamba. Choonadi cha Mau a Mulungu chidzapangitsa kuti anthu amasuke kwathunthu ndi kukhala pamtendere ndi Mulungu komanso iwo eni. Mneneri Yesaya analengeza za tsoka kwa amene

“ayesa zoipa zabwino, ndi

zabwino zoipa; amene aika mdima m'malo mwa kuyera, ndi kuyera m'malo mwa mdima” (Yesaya 5:20). Umu ndi mmene zinthu zilili m'dziko lathuli. Nkofunika kuti anthu a Mulungu aime m'chikondi komanso m'choonadi. Chiphunzitso chabwino cha Mau chidzitengedwa ngati muyeso woposa zonse. Zokhumba ndi zolinga za dziko lapansi sizikuloledwa kuti zilamulire popeza zikugwirizana ndi zikhalidwe ndi machitachita a gulu la anthu opanga za mathanyula.

Iwo amene akulimbikitsa za maukwati a amuna kapena akazi okhaokha akukhala ndi chikoka chachikulu, ndipo izi zikusokoneza mmene anthu timakhalira pachikhalidwe ndipo zikutsutsana ndi dongosolo la banja limene analikhazikitsa Mulungu. Mchitidwe wochita za mathanyula komanso kusinthana chibadwidwe chamunthu wamkazi kukhala mwamuna kapena mwamuna kukhala mkazi zikutengedwa ngati zovomerezeka kudzera mzofalitsa za atolankhani kapena zosangalatsa. Ngakhale kuti ena paokha sazilandira, komabe ambiri akuzilolera ndi kuzivomereza. Mau a Mulungu amaletsa kuchita za mathanyula, kusinthitsa chibadwidwe chachimuna kapena chachikazi, ndiponso kugonana ndi nyama. Ngakhale sikosangalatsa kutchula zinthuzi, komabe machitidwe a mathanyula ndi uchimo.

Chipangano Chakale chimaletsa kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha komanso kugonana ndi nyama

Chipangano Chakale chinkaletsa kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha. “Usamagonana ndi mwamuna, monga amagonana ndi mkazi; chonyansa ichi. Ndipo usamagonana ndi nyama iliyonse, kudetsedwa nayo; ...chisokonezo choopsa ichi. Musamadzidetsa nacho chimodzi cha izi; pakuti amitundu amene ndiwapirikitsa pamaso panu amadetsedwa nazo zonsezi” (Levitiko 18:22- 24). Inde Lamulo linkanena kuti anthu amene achita za mathanyula akuyenera kuti aphedwe (Levitiko 20:13-16).

Chiphunzitso cha Chipangano Chatsopano

Ngakhale kuti sitikukhalanso pansu pa maweruzo a chilamulo cha Mose, Chipangano Chatsopano chimaphunzitsanso momveka bwino kuti kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha ndi uchimo. Chifukwa chakuti kudzera m'chilakolako, anthu anayamba kudzilambira okha kuposa Mlengi, ndipo Mulungu anawapereka iwo ku zilakolako zoipa. “Akazi ao anasandutsa machitidwe ao a chibadwidwe akhale machitidwe osalingana ndi chibadwidwe: ndipo chimodzimidzinsu amuna anasiya machitidwe a chibadwidwe cha akazi, natenthetsana ndi cholakalaka chao wina ndi mnzake, amuna okhaokha anachitirana chamanyazi” (Aroma 1:24-28). Pa 1 Akorinto 6:9- 11 amatchula anthu amene sadzalowa mu ufumu wa Mulungu. Ena mwa iwo anali “akudziipsa ndi amuna.” Uku ndi kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha. Iwo amene “akuchita zoipa ndi amuna” alembedwa m'gulu la osamvera malamulo, osamvera, ndi osaopa Mulungu pa 1 Timoteo 1:9-10.

Chiwerewere ndi tchimo

Chigololo chamtundu uliwonse ndi machimo, kaya ndi dama kapena chigololo ndi mwamuna kapena mkazi. Akolose 3:5-6 amalangiza anthu “Chifukwa chake fetsani ziwalozi ...dama, chidetso, chifunitso chamanyazi, chilakolako choipa.” Paulo analangiza kuti: “Thawani dama....koma wachiwerewere achimwira thupi lake la iye yekha” (1 Akorinto 6:18). Iwo amene amachita chigololo, dama, chidetso, ndi zina zotero, sadzalowa mu

(Yapitirira pa tsamba 6)

(Kuchokera pa tsamba 5)

ufumu wa Mulungu (Agalatiya 5:19-21). Kukhumbana kwa matupi kumayenera kuchitika mu ukwati mokha komanso pakati pa mwamuna ndi mkazi basi.

Ukwati uli pakati pa mwamuna ndi mkazi

Ukwati wakhala ukuganiziridwa molakwika ndi kufotokozedwanso mu chikhalidwe chatu; koma kuyambira pachiyambi, Mulungu analenga mwamuna mmodzi ndi mkazi mmodzi, Adamu ndi Hava, kuti akhale pamodzi muukwati monga thupi limodzi (Genesis 2:18, 21-24). Mulungu sanalenge

amuna awiri kapena akazi awiri kuti akhale pachibwenzi ngati banja. Ukwati wa m'Baibulo unali ndipo udzakhalapo pakati pa mwamuna mmodzi ndi mkazi mmodzi. Yesu mwini anabwereza kunena choonadi chimenechi pa Mateyu 19:5-6: "Chifukwa cha ichi mwamuna adzasiya atate wake ndi amake, nadzaphatikizana ndi mkazi

wake, ndipo awiriwo adzakhala thupi limodzi? Chotero kuti salinso awiri koma thupi limodzi. Chifukwa chake ichi chimene Mulungu anachimanga pamodzi, munthu asachilekanitse." Mchitidwe wina uliwonse kapena kumanga banja pakati pa amuna kapena akazi okhaokha kuli kupotoza kwa dongosolo la Mulungu.



Kusankha kukhala mwamuna kapena mkazi

Kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha si zachilendo ndipo zakhalapo kwa zaka zikwizikwi. Komabe, masiku athu ano zikuoneka kuti zikuvomerezedwa, ndipo zapangitsa kuti zoipa zichulukire. Pamwamba posankha zokonda zao zokhudza kugonana ndi chilakalako chao, iwo ayambanso kusankha kuti akhoza kusintha chibadwidwe chao, pomwe amuna akukhala ngati akazi, akazi nakhala ngati amuna, ndipo choipa kwambiri, ena akusankha kukhala ngati nyama. Koma abale, dzikoli lafika poola motere mpaka kumavomereza ndi kulimbikitsa mchitidwe uwu wopanduka!

Genesis 1:27 imati "Mulungu ndipo adalenga munthu m'chifanizo chake, m'chifanizo cha Mulungu adamlenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mkazi." Zibadwidwe ziwiri zokha za anthu ndi zimene zikupezeka m'Malemba: amuna ndi akazi. Kukhala mwamuna kapena mkazi si chochita kusankha koma chotsatira cha chilengedwe. Tikatsutsana ndi izi kudzera mu kavalidwe, opareshoni ya kuchipatala ndi kumwa mankhwala zimanyozera mphatso yachilengedwe imene Namalenga anatipatsa. Anthu ochepa kwambiri amene mthupi lao zinthu zimene zimapangitsa kuti munthu azioneka ndi kuganiza ngati mwamuna kapena mkazi zinasokonekera. Koma sikuti aliyense ndi wotero. Nzomvetsa chisoni kuti ana ena amabadwa ndi zilema zamitundumitundu, koma ndi mmene zinthu zimakhallira m'dziko lathu lino. Kukhala ndi chilema chokhudza chibadwidwe siziyenera kukhala maziko akuti tichite zosemphana ndi dongosolo la Mulungu ndi kuyamba kunena kuti munthu payekha akhoza kusintha chibadwidwe chake.

Zochita za anthu osinthanitsa chibadwidwe chao zili zauchimo pamaso pa Mulungu ndipo Iye amaziletsa. Kuvala chovala chosiyana ndi chibadwidwe chako kukudzudzulidwa pa Duteronomo 22:5: "Mkazi asavale chovala cha mwamuna, kapena mwamuna asavale chovala cha mkazi; pakuti aliyense wakuchita izi Yehova Mulungu wanu anyansidwa naye." Ngakhale ndimeyi ikuletsa akazi kuvala zovala zachimuna makamaka zida zankhondo, koma ikunenanso kuti mwamuna asavale chovala chachikazi. Malemba a pa 1 Akorinto 6:9 akunena za "iwo okonda maonekedwe achikazi." Izi zikutanthauza amuna ovala zovala zopyapayala, komanso zopereka chikoka cha chiwerewere ndi maganizo olakwika kwa oziona. Kodi mwamuna wovala zovala za mkazi sangakhale m'gulu limeneli? Chibadwidwe chamunthu chikuyenera kuvomerezedwa ndipo wina asayesere kusintha, kusinthisa, kapena kuchita mosiyana.

Chiweruzo chaumulungu

Kulira kwa Sodomu ndi Gomora kukufikanso kumwamba masiku ano. Moto ndi sulfure zinatsanulidwa poweruza mizinda imeneyi chifukwa cha uchimo wao waukulu ndipo izi zikukhudzana ndi mutu tikukambiranawu (Genesis 19:1-14). Yuda 1:7 amachenjeza kuti: "Monga Sodomu ndi Gomora, ndi mizinda yakuizungulira, potsatana nayoyo, idadzipeka kudama, ndi kutsata zilakolako zachilendo, iikidwa chitsanzo, pakuchitidwa chilango cha moto wosatha."

Mzimu wa dziko lino

Popeza pali malingaliro ndi machitidwe opotoka okhudza za kugonana amene atizungulira m'nthawi ino, ndikofunikira kuti tisatengere mzimu wa dziko (1 Akorinto 2:12-13). "Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a panso pano: koma...mukazindikire chimene chili chifuniro cha Mulungu, chabwino, ndi chokondweretsa, ndi changwiwo." (Aroma 12:2).

Mulungu amakonda anthu ochita za mathanyula

Ngakhale kuti ziweruzo za Mulungu pa zoipa ndi chinyengo cha m'badwo uno zili zotsimikizika, Mulungu amakonda munthu aliyense payekha (Yohane 3:16). Mulungu amadana ndi tchimo koma amakonda wochimwayo. Yesu anafera ochimwa onse ndi ife tomwe. Mosatengera za moyo ndi tchimo limene wachita, "Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutsambitsa kutichotsera chosalungama chilichonse" (1 Yohane 1:9). Mulungu akhoza kutenga ochimwa oipitsitsa ndi kumuyeretsa. Yesu sanabwere kudzaweruzo koma kudzapulumutsa anthu ku machimo awo. "Chifukwa chake ngati munthu aliyense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano" (2 Akorinto 5:17).

Chipulumutso cha kwa anthu onse

Tiyeni tisataye mtima koma tikhalebe olimba m'choonadi cha Mau a Mulungu. Pemphererani iwo amene akodwa mu misampha yotchedwa ndi mdaniyo. Sikuti zonse zataika ayi, popeza mwa Yesu Khristu muli mphamvu yokusintha miyoyo. ■



Pokhala oyera mtima, kodi tikuyenera kuchita chiyani ndi anthu omwe amakhala moyo wopanga za mathanyula?

Anthu komanso mabanja akhoza kupezeka kuti ali pamavuto kuti adziwe mmene angachitire ndi anthu omwe amachita za mathanyula. M'chisankho chilichonse, nkofunika kwambiri kusunga mzimu ndi chikondi cha Khristu. Yesu anali bwenzi la ochimwa. Pa Mateyu 9:10-13, Afarisi anafunsa chifukwa chimene Yesu anali kudya ndi amisonkho ndi ochimwa. Yesu anayankha kuti, "Olimba safuna sing'anga ai, koma odwala. Koma mukani muphunzire nchiyani ichi, Ndifuna chifundo, si nsembe ai; pakuti sindinadze kudzaitana olungama, koma ochimwa."

Yesu sanali kuchita nao kapena kuchemerera khalidwe lao lochimwa; koma anali kuwafikira mwachikondi chifukwa cha miyoyo yao. Tiyenera kuwatenga anthu onse chikondi ndi ulemu monga zolengedwa za Mulungu, mosasamala kanthu za zosankha za moyo. Ngati tinyalanyaza kotheratu anthu amene akukhala mumdima, kodi iwo adzapeza bwanji chiyembekezo cha chipulumutso? Yesu anaphunzitsanso kuti tiyenera kukonda anzathu mmene timadzikondera tokha (Mateyu 22:39). Kodi mnzathu ndi ndani mu dziko lathu lauchimoli? Nkofunika kufananiza pakati pa kuwaonetsera chikondi koma osayanjana ndi uchimo waowo. Ngakhale pali kunyozedwa kwakukulu kwa makhalidwe onyansa a kugonana, kunyozedwa kumeneko kuyenera kukhala kwa mchitidwewo, osati kwa munthuyo.

Nkofunika kukumbukira kuti kukonda munthu sikutanthauza kuti mukugwirizana naye kapena kuti mumasekerera makhalidwe ake oipa.

Nthawi zambiri, zimandivuta kupita ku ukwati kapena chinkhoswe cha amuna kapena akazi okhaokha. Ngakhale kuti tikuwakhala anthuwa, sitingavomereze kapena kuchita nao chikondwerero chotere.

Nthawi zina kukhoza kukhala koyenera kuti tikhazikitse ndondomeko ndi kuchepetsa kuyanjana nao pofuna kusunga chiyero cha nyumba yathu, komanso makamaka kudziteteza wekha pamodzi ndi ana achichepere ku zinthu zoipa zimene zingawakope. Nthawi zonse, chilichonse chimene chikunenedwa ndi kuchitidwa chichitike mwa mzimu wa Khristu. Koma chofunika koposa, pemphererani chipulumutso chao. ■

Kodi ndingatani ngati ndikumakopeka ndi anzanga a chibadwidwe chofanana?

Mdani wagwira ntchito molimbika kuti zogonana amuna kapena akazi okhaokha zioneke ngati ndi mmene zinthu zimakhala. Ngati wina akopeka ndi munthu yemwe ali wofanana naye chibadwidwe, pemphero likhoza kukhala chida chachikulu pofuna kugonjetsa mdani ndi thupi. Pali kumasuka ku uchimo kwaumulungu ndipo mwa Khristu tikhoza kugulula mphamvu ya mayesero. Tikhoza kumasulidwa ku mizimu ya chilakolako chathupi. Pamene kusokonekera pankhani za kugonana kukuchulukirachulukira, mayesero adzikhala ochuluka. Zochitika, chilengedwe, ndi zizolowezi zachilengedwe zikhoza kupangitsa anthu ena kukhala osatetezeka kuposa ena. Ndikofunika kukumbukira kuti mayesero si tchimo; koma kugonjera ku tchimo. "Sichinakugwerani inu chiyeso koma cha umunthu; koma Mulungu ali wokhulupirika, amene sadzalola inu kuyesedwa koposa kumene mukhoza; koma pamodzi ndi chiyeso adzaikanso populumukirapo, kuti mudzakhoze kupirirako" (1 Akorinto 10:13).

Ndikofunikiranso kwambiri musadzipereke ku zinthu zimene zingakukopeni kuchita nao zoipa. Musaonere zinthu kapena kucheza ndi anthu omwe angakukopeni kapena kukulitsa mayesero anu kuchita muchite zimenezi. Thawani zinthu zonse zomwe zingapangitse kuti mukhumbire kuyanjana nao ochita zimenezi. Pakulimbana kwanu, pitirizani kumenyana. Tsiku lililonse muzipempha kwa Mulungu kuti akuthandizeni kuika mtima wanu ndi maganizo anu pa zinthu zabwino ndi zoyera. Mukhale ndi anthu amene ali oyera mtima ndipo akhoza kukuthandizani kukula mu kuyenda kwanu ndi Mulungu.

Ngati simuli pabanja, musafune kukwatira kapena kukwatiwa ncholinga chongofuna kukwaniritsa chikhumbitso chanu pongokopeka ndi munthu wina amene ali wa chibadwidwe chimodzi ndi inuyo. Chinthu chimenecho chidzakutsatani mubanja ndipo zidzabweretsa mavuto aakulu. Choyamba gonjetsani ndipo kenaka mufunefune kuti Mulungu akupatseni mnzanu wa banja womuopa iye monga mwa chifuniro cha Mulungu.

Mukhale olimbikitsidwa. Pali mphamvu yogonjetsa tchimo ndi mayesero; Mulungu ali ndi malo achigonjetso ndi mtendere kwa inu. ■



KODI MUKUDZIWA?

“Malingana ndi kafukufuku wa Pew Research Center wa anthu okwana 12,147 a ku America adachitika mu chaka cha 2022, anthu 7 mwa 100 aliwonse a mdzikolo amachita za mathanyula kapena amatha kugonana ndi mwamuna kapena mkazi mnzao komanso nkukagonana ndi wina wosiyana naye chibadwidwe. Pafupifupi 17% ya achinyamata osapitirira zaka 30 amadziwika kuti amachitanso mchitidwe umenewu kuyerekeza ndi 8% ya iwo a zaka zapakati pa 30 mpaka 49. Ndipo 5% ndi ya iwo a azaka zapakati pa 50 mpaka 64 ndipo 2% ndi ya iwo azaka 65 kapena kuposerapo. [Brown, Anna. June 23, 2023. www.pewresearch.org.]

“Mwa maiko 30 amene kunachitidwa kafukufuku, 3% ya anthu anavomereza kuti amagonana ndi mwamuna kapena mkazi mnzao, ndipo 4% amagonana ndi amuna kapena akazi anzao kuphatikizapo kugonananso ndi wina wosiyana naye chibadwidwe, pamene 1% amagonana ndi china chilichonse, kaya ndi mwamuna kapena akazi kapenanso nyama, ndipo 1% samakhala ndi chikhumbokhumbo chofuna kugonana ndi wina aliyense.” [www.ipos.com (2023)]




**Mau a
Nyengo
Yake**

NYAMULIRANANI ZOTHODWETSA WINA NDI MNZAKE

Nyamuliranani zothodwetsa, ndipo kotero mufitse chilamulo cha Khristu. — Agalatiya 6:2

Tikukhala m’dziko loonongeka chifukwa cha uchimo. Anthu akulimbana ndi makhalidwe achitaiko, zizolowezi zoipa, ndi moyo wa zilakolako zoipa. Iwo ali osungulumwa ndipo amafunitsitsa atadziwika, navomerezeka ndi ena komanso kukhala pa mtendere. Maubale a mabanja akuguga ndipo mabanja akutha. Ana akukumana ndi zikoka zoipa ndi zowapsinja kuposa kale. Mavuto a thanzi la m’maganzo komanso a m’maligaliro akuwonjezeka. Mmene dziko likuyendera zikuoneka kuti miyoyo yambiri ikuonongeka.

Ngakhale zikuoneka kuti palibe chabwino chilipo, pali chiyembekezo chowala mwa Yesu Khristu. Kutsogoloko tidzakalowa Kumwamba kumene sikudzakhalanso kuvutika. M’dziko lino muli mazunzo, koma kudzera mwa Yesu, tili ndi kuwala, chiyembekezo komanso mtendere. Tili ndi china chodabwitsa chakuti tigawane nawo anthu amene akuvutika. Zinthu za dziko lino lapansi sizikupereka yankho ku mavuto amene anthu ali nao; ndipo mmalo mwake zikunka ziipiraipira. Tiyeni tilalikire momasuka za chiyembekezo chaulemerero cha uthenga wabwino.



Malemba amatiphunzitsa kuti “Nyamuliranani zothodwetsa.” Zimenezi zikutanthauza kusenza, kunyamula, kupirira moleza mtima zothodwetsa za ena. Anthu amene asweka amafunikira chikondi, chisamaliro, ndi kuwamvetsetsa. Sitingathe kuwakonza anthu, koma titha kuwathandiza. Tikhoza kumvetsera, tikhoza kupemphera, tikhoza kuwapatsa chiyembekezo, ndipo chachikulu kuposa zonse tikhoza kuwalozera iwo kwa Mpulumutsi, amene akhoza kuchita zimene munthu sangathe kuchita.

Kunyamula zothodwetsa za ena sikophweka nthawi zonse, koma awa ndi maitanidwe athu ndi udindo wathu. Anthu omwe akupwetekedwa akhoza kumva kupweteka; akhoza kuwatafulira anthu amene amawakonda. Pamene mukusenza zothodwetsa za anthu, kumbukirani kuti mukhoza kuvulazidwa. Mukadzipereka chifukwa cha ena, nthawi zina iwo akhoza kukupwetekani ndi mau komanso machitidwe ao. Yang’anirani zimene iwo akunena kapena kuchita ndikulingalira za kusweka kwao. Kodi adzakhala kuti ngati inu muwasiya iwo?

Monga Mulungu wakhala akuleza nafe mtima ndi wokhulupirika kwa ife, tiyeni tikwaniritse chilamulo cha Khristu ndipo tionetse kuleza mtima ndi chikondi chomwecho kwa ena amene akuvutika kupeza njira yao. Tiyeni tiziwaonetsera Khristu mwa chikondi ndi chisamaliro chathu. Ambuye Yesu akudalitseni aliyense wa inu pamene mukunyamula zothodwetsa za ena. ■

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE